# MOYO WA KHRISTU

## GAWO LOYAMBA

BUKU LA M'NDANDANDA WA OFALITSA A T.E.E.

Karagama Gadzama, Mary Lar
Lilian Sampson, Dick ndi Kitty Winfield

# MOYO WA KHRISTU

## GAWO LOYAMBA

BUKU LA M'NDANDANDA WA OFALITSA A T.E.E.

Karagama Gadzama, Mary Lar
Lilian Sampson, Dick ndi Kitty Winfield

# MOYO
# WA
# KHRISTU

## GAWO LOYAMBA

Karagama Gadzama, Mary lar
Lilian Sampson, Dick ndi Kitty Winfield

Lomasulidwa ndi T.E.E.
Baptist T.E.E.
P.O. Box 467
Lilongwe, MALAWI

Losindikizidwa ndi:
Baptist Publications
P.O. Box 444
Lilongwe, MALAWI

ZOLEMBEDWA NDI A EVANGEL PUBLISHING HOUSE - 1977

Udindo wolemba buku ili unapatsidwa kwa a Evangel Publishing House TEXT - AFRICA povomerezana ndi amene analemba bukuli. Bukuli ndi lochitidwa ndi mgwirizano wa mu Afrika pa utsogoleri wa TEXT - AFRICA womwe anagwira ntchito mogwirizana ndi a AEAM THEOLOGICAL COMMISSION.

Simuyenera kutengedwa gawo kapena ndime m'bukuli popanda chilolezo cholembedwa ndi a Evangel Publishing House.

Chilolezo chotanthauzira bukuli m'zinenero zina chidzaperekedwa ngati opemphawo atalembera ku Evangel Publishing House. Ndi kulakwira malamulo a anthu olemba ngati mungotanthauzira bukuli popanda chilolezo cholembedwa.

Pamene mukulemba pempho lofuna chilorezo chotanthauzira bukuli, chonde tchulani dzina lanu, mpingo wanu kapena mishoni, keyala yanu ya thunthu, ndi njira ya katanthauzidwe kamene mugwiritsa ntchito. Pamene mwatsiriza kutanthauzira buku limodzi ndi kusindikizidwa litumizeni kwa ofalitsa ndi oyang'anira ntchitoyi (Fred Holland, 135 N. Oakland, Pasadena, ca. 91101, U.S.A.) Muyenera kuphunzira malangizo a katanthauzidwe ndi bungwe lanu la matanthauzidwe musanayambe ntchito yotanthauzira. Zolemba za machenjezozi zimapezeka ku nyumba zofalitsira ndipo zimapereka malangizo ambiri kwa otanthauzira maphunziro amenewa.

Ndime za buku limeneli zinatengedwa m'buku Lopatulika la Revised Standard Vession m'kalembedwe ka chi America. Koma ndime zina zinatengedwa m'masipelo a chizungu.

Buku lolembedwa m'Chichewa movomerezedwa ndi Evangelical Publishing House.

Evangel Publishing House
P.O. Box 1015
Kisumu, KENYA.

# MAWU OYAMBA

Ili ndi buku lina lofunika kwambiri lophunzirira ku nyumba lothandiza atsogoleri a mpingo. Bukuli limaphunzitsa za gawo loyamba la moyo wa Yesu Khristu. Limaonetsa mmene Khristu analili munthu wofunika kwambiri pamene anali pa dziko lapansi. Limaonetsa mmene Mwana wa Mulungu anatiphunzitsira ife makhalidwe. Pali buku linanso limene limationetsa za mmene Khristu anafera ndi kuukanso kwa akufa.

Buku limeneli lili monga mphunzitsi. Limalankhula kwa inu. Limakuuzani za zinthu zoyenera kuchita. Ngati mukufuna kuphunzira, liwerengeni mosamalitsa. Lembani mayankho onse. Chitani ntchito yonse. Gwiritsani ntchito maphunziroŵa mu mpingo wanu. Njira imene maphunziro ameneŵa analembedwera amatchedwa PI kapena kuti programmed Insruction.

Mabuku ameneŵa ndi a atsogoleri a mpingo ndi ena ogwira ntchito mumpingomo kuti aziphunzirira kunyumba. Ophunzira ayenera kumakomana ndi atsogoleri sabata ndi sabata kuti azikambirana za maphunziroŵa. Kugwiritsa ntchito mabukuŵa m'njira yotere imatchedwa T.E.E. kapena kuti Theological Education by Extention. Maphunziro a T.E.E. amaphunzitsa atsogoleri a mipingo kunyumba zawo.

Mipingo yambiri yofalitsa Uthenga mu Afrika ili kugwirira ntchito pamodzi kuti ikupatseni mabuku ameneŵa. Phunziro lililonse ndi lolembedwa mosamalitsa bwino. Ndipo limayesedwa pofuna kutsimikiza kuti likuphunzitsadi bwino. Timakhala mosamalitsa kwambiri kuti tizinena zomwe Buku Lopatulika limanena. Mipingo yonse imene imathandizana ndi mabuku ameneŵa imavomereza Buku Lopatulika monga Mawu a Mulungu Oonadi. Anthu amaphunzitsa maphunziro a Buku Lopatulika m'nuira zosianasiyana ndi kutsatira Buku Lopatulikalo mwa kukhulupirira pa Yesu monga njira yokhayo ya chipulumutso, timaŵalandira monga abale athu. Timayesetsa kukhala ndi anthu a mipingo yosiyanasiyana kuti aone m'maphunziroŵa ngati ali olakwika. Choncho maphunziro onseŵa amatsatira Buku Lopatulika. Ena mwa maphunziroŵa timachepetsa ndi cholinga chakuti mabukuŵa azikhala ogwirizana kuti mipingo yonse iziŵagwiritsa ntchito. Anthu ena amatilembera pochitira ndemanga za mabuku ameneŵa. Chimenechi ndi chinthu chabwino chifukwa timamva zomwe zili zabwino ndi komwe kuli mavuto. Tidzakhala okondwa ngati inu mudzatilembera ife za ntchito yanu ndi zimene mukuganizira za mabukuŵa.

Anthu ambiri anathandiza polemba buku la Moyo wa Khristu, Gawo Loyamba. Maphunziro ameneŵa amalembedwa, ndi kuyesedwa, ndi kulembedwanso. Karagama Gadzama ali ndi certificate yochokera ku Theological College of Northern Nigeria. Iye tsopano ali kuphunzitsa pa Kulp Bible School mu Borno State, Nigeria. Iye ndi msungi chuma wa mpingo wotchedwa Ekklesiyar Yan'uwa A Nigeria.

Mary Lar ndi m'Nigeria amene wakhala ali kuphunzitsa m'sukulu za boma ndi ku Theological College of Nigeria. Iye analandira Certificate kuchokera ku College of All Saints, Tottenham, England, ndipo ali ndi

B.A. m'maphunziro kuchokera ku Ahmadu Bell University ya ku Zaria. Pakali pano iye ali kuphunzitsa komanso ndi mkulu wa sukulu ndiponso amachita pulakitisi ku Alewanga Advanced Teachers College.

Dick ndi Kitty Winfield akhala zaka zisanu ndi zinayi mu Nigeria Nthaŵi yonseyi akhala ali kuphunzitsa ku Kulp Bible School mu Borno State. Dick ali ndi M.Div. kuchokera ku Ashland Theological Seminary. Kitty ali ndi B.A. kuchokera ku Ashland College.

Phunzirani mosamalitsa bwino buku limene aphunzitsiwa analemba za Khristu. Mudzaphunzira zambiri za moyo wanu ndi ntchito kuchokera kwa iwo.

Abwenzi anu mwa Khristu,
Fred ndi Grace Holland
TEXT - AFRICA project editors

135 N. Oakland
Pasadena, CA 91101

MENE MUNGAGWIRITSIRE NTCHITO BUKU ILI

Buku limeneli ndi mphunzitsi wanu. Lizikuphunzitsani phunziro tsiku ndi tsiku. Limvereni mosamalitsa zimene bukuli likunena monga mmene mungamvere mphunzitsi wanu. Pamene mphunzitsi wanu akuuzani kuti mutenge Buku Lopatulika ndi kuwerenga, inu simungomuyang'anitsitsa ayi. Mumatenga Buku Lopatulika ndi kuliwerenga. Chimenechi ndi chimene muyenera kuchita ndi buku limeneli.

Mkalasi mphunzitsi amauza ophunzira kanthu kena. Iye amafotokoza bwinobwino. Ndipo iye amafunsa mafunso. Ngati ophunzirawo ayankha bwino, mphunzitsiyo amapitiriza ndi phunziro lina. Buku lino limagwiritsidwa ntchito mwa njira yomweyo. Poyamba limakupatsani gawo laling'ono la maphunziro. Ndipo limakufunsani mafunso. Ngati mutawerenga bwino, mukhoza kuyankha bwino. Ngati mwayankha bwino zimasonyeza kuti mwamvetsetsa. Chimakuthandizaninso kuti mukumbukire zimene mwawerenga.

Nthaŵi zonse mukhoza kumayankha mayankho olondola. Ngati muli wosakhutira ndi yankholo werenganinso maphunziro ochokera mufunso lotsiriza. Ngati simuli kutsimikizabe, lembani yankho limene mungalitsimikize kuti ndilo labwino. Ndipo pitirizani. Pamene mukupitiriza kuchita maphunziroŵa mudzaona kuti muli kuyankha bwino. Koma ndikofunika kwambiri nthaŵi zonse kuti muzilemba yankho lanu labwino munsanawerenge gawo lina la phunziro. Zidzakuthandizani ngati mutagwiritsa ntchito pepala kuti muphimbe mbali ina ya tsamba pamene mukuwerenga.

Sunthani pepalalo pa mnzere wochindikira umene umene umaoneka motere========. Ŵerengani maphunziro ndipo yankhani mafunso. Ndipo sunthani pepala pansi pa nzere wina wochindikara. M'njira imeneyi simudzawerengeratu mayankho musanakonzekere. Pamene mukuwerenga mayankho, ganizirani za yankholo. Ndipo lidzakukonzani ngati muli kuphunzira molakwa.

Lidzakutengerani masabata khumi kuti mutsirize buku limeneli. Muzichita phunziro limodzi tsiku ndi tsiku kwa masiku asanu sabata ili yonse. Musayesa kuchita maphunziro aŵiri kapena atatu pa tsiku limodzi. Mafunso otsirizira a tsiku lililonse ndiye ofunika koposa. Amaonetsa zimene mphunzitsi akufuna kuti muzikumbukira. Zimenezi timazitcha kuti zolinga za buku. Kumapeto a sabata, mukhoza kudziŵa kuti mwaphunzira bwino ngati mutayankha mafunso ameneŵa.

Buku limeneli liyenera kugwiritsidwa ntchito pa misonkhano ya sabata iliyonse. Muyenera kukhala ndi mtsogoleri amene angakuthandizeni ndi mavuto anu. Mtsogoleri ayeneranso kukuthandizani kuti muzikambirana ndi ophunzira ena zimene mwaphunzira. Ngati simunaphunzire maphunziro musanapite kukalasi, inu simukamvetsetsa zimene zili kukambidwa.

ZA MKATIMU


SABATA LOYAMBA: KUBADWA KWA KHRISTU

Tsiku Loyamba: Kodi ndi chifukwa chiyani tikuphunzira moyo wa Khristu? ........ 11
Tsiku Lachiŵiri: Khristu pa chiyambi ........................... 17
Tsiku Lachitatu: Kubadwa kwa Khristu M'Betelehemu ............. 21
Tsiku Lachinayi: Mngelo achezera Mariya ......................... 27
Tsiku Lachisanu: Mngelo anauza abusa ........................... 32

SABATA LACHIŴIRI: UKHANDA WA KHRISTU

Tsiku Loyamba: Kucheza kwa anzeru akummaŵa .................. 38
Tsiku Lachiŵiri: Herode ayesa kupha Yesu ....................... 45
Tsiku Lachitatu: Mnyamata Yesu apita ku Yerusalemu ............ 50
Tsiku Lachinayi: Ntchito ya Yohane Mbatizi ..................... 56
Tsiku Lachisanu: Malo amene Yesu anakhala ndi kuphunzitsa ...... 62

SABATA LACHITATU: KHRISTU AKONZEKERA NTCHITO YAKE

Tsiku Loyamba: Yesu anabatizidwa kuti achite chifuniro cha Mulungu. ....... 74
Tsiku Lachiŵiri: Ubatizo wa Yesu ............................... 80
Tsiku Lachitatu: Mayesero a Yesu ............................... 86
Tsiku Lachinayi: Mayesero a Yesu amatithandiza ................. 93
Tsiku Lachisanu: Kubwereza ..................................... 100

SABATA LACHINAYI: KHRISTU AYAMBA NTCHITO YAKE

Tsiku Loyamba: Chozizwitsa choyamba ........................... 104
Tsiku Lachiŵiri: Yesu anauza Nikodimo za kubadwa kwatsopano .... 111
Tsiku Lachitatu: Iye anauza Nikodimo za moyo wosatha ........... 118
Tsiku Lachinayi: Iye apereka madzi amoyo kwa Msamariya ......... 124
Tsiku Lachisanu: Iye akanidwa ku Nazarete ...................... 130

SABATA LACHISANU: KHRISTU ATHANDIZA ANTHU

Tsiku Loyamba: Yesu Khristu ali ndi mphamvu yoposa ziŵanda ... 137
Tsiku Lachiŵiri: Yesu aonetsa kuti Iye amasamalira anthu ....... 143
Tsiku Lachitatu: Khristu ali ndi mphamvu yokhululukira machimo . 150
Tsiku Lachinayi: Iye aphunzitsa za kupembedza koona ............ 154
Tsiku Lachisanu: Yesu aphunzitsa za tsiku lopumula ............. 160

SABATA LACHISANU NDI CHIMODZI: KHRISTU NDI OPHUNZIRA AKE

Tsiku Loyamba: Iye aitana ophunzira khumi ndi aŵiri apadera ... 167
Tsiku Lachiŵiri: Ophunzira oona amakonda ndi kumvera Yesu ...... 174
Tsiku Lachitatu: Iye asandutsa ophunzira ake kukhala asodzi ..... 180
a anthu.
Tsiku Lachinayi: Khristu adzudzula ophunzira ake pamene ......... 186
achita zolakwa.
Tsiku Lachisanu: Kubwereza .................................. 195

SABATA LACHISANU NDI CHIŴIRI: KHRISTU APHUNZITSA PA PHIRI

Tsiku Loyamba: Ife timadalitsika tikamavutika ................. 195
Tsiku Lachiŵiri: Akhristu ndi kuwala ndi mchere wa dziko ........ 202
lapansi.
Tsiku Lachitatu: Musakwiye kapena kuchita chigololo mumtima ..... 208
mwanu.
Tsiku Lachinayi: Kukonda ndi kupempherera adani anu ............. 215
Tsiku Lachisanu: Tiyenera kupemphera mtseri ndi ................. 222
kukhululukira.

ABATA LACHISANU NDI CHITATU: KHRISTU APHUNZITSA ZINA ZAMBIRI PA PHIRI

Tsiku Loyamba: Ife sitingathe kutumikira Mulungu ndi chuma .... 229
Tsiku Lachiŵiri: Mulungu adzayankha mapemphero athu ............. 236
Tsiku Lachitatu: Tiyenera kuchenjera ndi aneneri onyenga ........ 243
Tsiku Lachinayi: Kukhulupirira Khristu kuli monga kumanga........ 250
nyumba pa thanthwe.
Tsiku Lachisanu: Yohane Mbatizi abweretsa makaiko ake kwa Yesu .. 256
Kubwereza

SABATA LACHISANU NDI CHINAYI: KHRISTU APHUNZITSA ANTHU AMBIRI

Tsiku Loyamba: Khristu mnyumba ya Simoni ...................... 263
Tsiku Lachiŵiri: Nthano ya namsongole ........................... 270
Tsiku Lachitatu: Ufumu wa Mulungu ufanana ndi chuma ............. 277
Tsiku Lachinayi: Adaonetsa mphamvu yake pa zinthu zonse ......... 283
Tsiku Lachisanu: Khristu atuma ophunzira kuti akalalikire ....... 290

SABATA LA KHUMI: KHRISTU MKATE WA MOYO

Tsiku Loyamba: Anadyetsa anthu zikwi zisanu (500) ............ 297
Tsiku Lachiŵiri: Iye ayenda pa nyanja ndi kutontholetsa ........ 303
Namondwe.
Tsiku Lachitatu: Idyani thupi langa ndipo imwani mwazi wanga ... 310
Tsiku Lachinayi: Khumi ndi aŵiri anatsala pamene ambiri ........ 317
anabwerera m'mbuyo.
Tsiku Lachisanu: Kubwereza ....................................... 324

SABATA LOYAMBA: KUBADWA KWA KHRISTU
TSIKU LOYAMBA : KODI NDI CHIFUKWA CHIYANI TIKUPHUNZIRA MOYO WA KHRISTU?

1. Zaka zambiri zapitazo m'dziko lathu munali mfumu yaikulu. Mfumuyi inabadwira m'mudzi waung'ono wa mu Afrika. Pamene inakula inapatsidwa ufumu. Iyo inali kuweruza bwino anthu ake. Inali yolimba mtima ndi ya mphamvu komanso inali yachifundo. Pamene inamwalira, anthu ake anali ndi chisoni kwambiri.

Kodi inu mumakonda kuphunzira za anthu a akulu otere? ____ ________

==========

2. Buku lino ndi la za anthu a akulu otero. Maphunziro amene mukhale mukuphunzira si za mfumu yamu Afrika ayi. Koma ndi onena za munthu wa mkulu. Iyeyu dzina lake anali Yesu. Iye anabadwira m'mudzi waung'ono ndipo anali kutchedwa Mfumu. Anali wolimba mtima ndi wamphamvu, komanso anali wachifundo. Pamene Iye anafa, anthu ambiri anali ndi chisoni. Koma pasanapite nthaŵi iwo anakondweranso. Iwo anakondwera chifukwa munthu ameneyu anakhanso ndi moyo.

Kodi muli kuganiza kuti ndikofunika kwa Mkhristu kuphunzira za moyo wa Khristu?

________________

==========

3. Ife tikuganiza kuti ndi kofunika. Tikufuna kuti inu mukondwere ndi phunziro limeneli chifukwa likuthandizani. Pali zifukwa zambiri zimene Akhristu ayenera kuphunzira za Khristu. Tikuphunzitsani zifukwa zambiri zimene Akhristu ayenera kuphunzira za Khristu. Tikuphunzitsani zifukwa zitatu. Potsiriza pa phunziroli mulembe ziŵiri mwa izo.

Tiyenera kuphunzira moyo wa Khristu:
(1) Kuti timudziwe bwino Mulungu.
(2) Kuti tizikhoza kutsata chitsanzo cha Khristu
(3) Kuti tikhoza kuuza ena za Khristu.

Ife tikupemphera kuti tsopano mudzakhala Mkhristu wabwino monga mudayenera kukhalira. Tsopano yambani mwadzipempherera nokha. Pempherani kuti mudziŵe bwino Mulungu mphunziro lino.

==========

4. Chipangano Chakale chimapereka ulosi wa kudza kwa Yesu. Koma za moyo wa Yesu unafotokozedwa m'Chipangano Chatsopano. Mabuku anayi oyamba a m'Chipangano Chatsopano amanena za moyo wa Khristu. Mabuku

ameneŵa amatchedwa Uthenga. Buku limodzi mwa mabuku a Uthenga ophunzira amanena mawu awa kwa Yesu.

Yohane 14:8-9:

> "Ambuye, tionetseni ife Atate, ndipo chitikwanira."
> Yesu ananena naye, "... Iye amene wandiona Ine waona Atate; unena iwe bwanji, mutionetsere atate?"

Ganizirani mofatsa za ndime zimenezi. Pamene ife tiyang'ana kwa Yesu, kodi wina ndani amene timamuona?

________________________________________

===================================================================

5. Ife timaona Atate. M'mawu a Khristu ameneŵa, "Atate" amatanthauza Mulungu. Pamene tikuphunzira za Khristu tikhoza kumudziŵa bwino Mulungu. Anthu ambiri amafuna kudziŵa zambiri za Mulungu. Yesu ananena kuti ngati tikuona Iye ndiye kuti timaona Mulungu. Pamene ife tikudziŵa za Khristu ndiye kuti timadziŵanso za Mulungu.

Khristu anakonda anthu onse. Kodi zimenezi zimatiuza chiyani za Mulungu?

____________________________________________________________

____________________________________________________________________

===================================================================

6. Zimatiuza kuti Mulungu amakondanso anthu onse. Popeza Khristu anakonda, tidziŵa kuti Mulungu amakonda. Khristu amationetsa ife Mulungu. Zinthu zimene Khristu anali kuchita zinali ntchito za Mulungu. Zinthu zimene Iye ananena zinali Mawu a Mulungu.

Kodi ndi moyo wa yani umene tikuphunzira pofuna kuti tim'dziŵe Mulungu bwino?

____________________________________________________________

===================================================================

7. Tikuphunzira moyo wa Khristu. Buku Lopatulika limatiuza za "Chikondi cha Mulungu." M'moyo wa Khristu amationetsa ife za chikondi cha Mulungu. Khristu anakonda ana, ochimwa, osauka, ndi odwala. Iye anali kukonda amene sanali kukondedwa ndi anthu ena. Tidziŵa kuti Mulungu amakonda chifukwa Khristu anakhala m'moyo wachikondi.

Garba ndi Mkhristu amene akuphunzira mabuku a Uthenga. Iye akuphunzira za moyo wa Khristu pamene anali pa dziko lapansi.

Kodi Garba akuphunziranso za yani poonjezera za Khristu?

______________________________

---

8. Garba akuphunzira za Mulungu. Pali zifukwa zitatu zimene tiyenera kuphunzira za moyo wa Khristu. Lembani chifukwa choyamba ndipo werengani ziŵiri zinazo.

(1) ______________________________

(2) Kuti tikhoza kutsata chitsanzo cha Khristu.
(3) Kuti tikhoze kuuza ena za Khristu.

---

9. Timaphunzira za moyo wa Khristu kuti tim'dziŵe bwino Mulungu. Chimenechi ndicho cholinga choyamba. Tsopano tiyeni tionetsetse mosamalitsa bwino pa chifukwa chachiŵirichi. Tiyenera kuphunzira moyo wa Khristu (2) kuti tikhoze kutsata chitsanzo cha Khristu.

Kodi dzina lanu lili ndi tanthauzo? Ambiri mwa ife amuno mu Afrika timadziŵa tanthauzo la maina athu. Dzina lakuti Akhristu limafotokoza za kanthu kena. Lili ndi dzina la Khristu mkati mwake.

Kodi ndi munthu uti amene Akhristu amamutsata? ______________

---

10. Mkhristu ayenera kutsata Khristu. Mwina mudaona mnyamata wamng'ono akuyesera potsata mapazi a atate wake. Mnyamata anali kufuna kukhala monga atate wake. Iye anali kufuna kutsata chitsanzo cha atate ake. Buku Lopatulika limatiuza kuti tiziyenda m'mapazi a Khristu. Ngati tichita zimenezi tidzatha kukhala monga Iye.

1 Petro 2:21:

Pakutinso Khristu anamva zoŵaŵa m'malo mwanu,
nakusiyirani chitsanzo kuti mukalondole mapazi ake.

Hannatu anali mayi wa Chikhristu. Ndipo mayi wina anamunenera bodza. Poyamba Hannatu anakalipa. Iye anafuna kubwezera kwa mayi winayo. Ndipo iye anakumbukira Khristu. Iye anakumbukira kuti Yesu sanabwezere chilichonse kwa anthu amene anali kumupha.

Kodi Hannatu anayenera kuchita chiyani potsata chitsanzo cha Khristuyo?

______________________________

---

11. Iye ayenera kukhululukira mayi winayo pofuna kutsata chitsanzo cha Khristu. Kodi inu mukhoza kutsata chitsanzo cha wina ngati simukumudziŵa bwino? Ayi, simungathe. Poyamba muyenera kuphunzira za iye. Muyenera kuphunzira zimene iye amachita. Muyenera kuphunzira zimene ananena. Muyenera kuphunzira moyo wake ngati inu muli kufuna kutsata chitsanzo chake.

Ine ndikufuna kutsata chitsanzo cha Yesu. Kodi ndichite chiyani kuti ndidziŵe za Iye?

__________________________________________

===========================================================

12. Ndiyenera kuphunzira za moyo wake. Pamene Yesu anali padziko lapansi, Iye anationetsa zinthu zabwino zambiri. Koma ife tiyenera kuphunzira kuti tidziŵe kuti zinthuzi ndi zotani. Pamene tili ndi mavuto tiyenera kuganizira za moyo wa Khristu. Tiyenera kufunsa kuti tione zimene Iye anatichita ndi vuto limeneli. Tiyenera kufunsa kuti tione zomwe Iye ananena za vuto limeneli. Yesu anali mphunzitsi wachitsanzo chabwino. Ife tiyenera kumutsata Iye.

Kodi mukuganiza kuti ndi kwapafupi kutsatira chitsanzo cha Khristu?

________________________________________________________

Chifukwa chiyani? ____________________________________________

===========================================================

13. Tidzakambirana za yankho lanu mkalasi.

Tsopano lembani zifukwa ziŵiri zomwe tiyenera kuphunzirira moyo wa Khristu.

(1) ______________________________________________

(2) ______________________________________________

(3) Kuti tikhoza kuuza ena za Iye.

===========================================================

14. Ife timaphunzira moyo wa Khristu (1) kuti tikhoze kudziŵa za Mulungu. (2) kuti tikhoze kutsata chitsanzo cha Khristu. Palinso chifukwa china.

Tatiyeni tinene kuti mtsogoleri wa dziko lanu ali kubwera mu mzinda wanu. Imeneyi ndi mbiri yabwino! ndipo inu mumakhala anthu oyamba mu

mzindamo kumva za zimenezi.

Kodi inu mukhoza kubisa mbiri yabwinoyi kapena kuŵafotokozera anthu ena?

---

===========================================================

15. Ndi zoona kuti mukhoza kunena za mbiri yabwinoyi. Timakonda kugaŵira ena zinthu zabwino. Monga Akhristu, ife tili ndi mbiri yabwino. Mbiri yabwino ndi ya za Khristu. Zinthu zimene Yesu anachita ndi zimene anaphunzitsa ndi mbiri yabwino kwa anthu onse.

Kodi tiyenera kuchita chiyani ndi mbiri yabwino ya Khristu?

---

==========  ===============================================

16. Tiyenera kuuza ena za mbiriyo. Ngati titauza anthu anu kuti munthu wamkulu ndi wamphamvu ali kubwera kudzacheza, kodi iwo akhoza kuchita chiyani? Iwo akhoza kufunsa mafunso ena. Iwo akhoza kufunsa kuti akubwera liti? Iwo akhoza kufunsa kuti akubwera ku mzindawo kudzatani. Iwo akhoza kufunsa mmene angadzamulandirire munthu ameneyu. Iwo akhoza kufuna kudziŵa mayankho.

Zimenezi zidzaonekanso pamene mukuuza ena za Khristu. Iwo adzakufunsani mafunso aza Iye.

Kodi ophunzira amakonzekera bwanji pofuna kuyankha mafunso a mayeso?

---

Kodi inu muyenera kuchita chiyani kuti muyankhe mafunso aza Khristu?

---

===========================================================

17. Muyenera kuphunzira moyo wa Khristu. Mafunso ayenera kuyankhidwa. Muyenera kugaŵira ena zimene inu mukuzidziŵa. Muphunziro lino tiphunzira mosamalitsa bwino za moyo wa Khristu. Tigwiritsa ntchito Mateyu Marko, Luka, ndi Yohane, ndi buku la phunziroli.

Kodi cholinga chachitatu ndi chiyani pofuna kuphunzira moyo wa Khristu?

(1) Kuti mum'dziŵe bwino Mulungu.
(2) Kuti titsate chitsanzo cha Khristu.

(3) ______________________________

==========================================================================

18. Timaphunzira moyo wa Khristu kuti tikhoze kuuza ena za Iye. Buku Lopatulika limatiuza kuti Mzimu Woyera adzatithandiza ife kuuza ena za Khristu. Koma ife tiyenera kuchita zimene tingathe kuti tidzikonze tokha. Maphunziro ameneŵa adzatithandiza ife. Tiyeni tiphunzire moyo wa Khristu mosamalitsa. Tiyeni tipemphe thandizo la Mzimu Woyera.

Kodi inu mumafuna kudziŵa zambiri za moyo wa Khristu? ______________

==========================================================================

19. Ngati mwalemba kuti Inde, ndiye kuti takonzekera kukhala ndi nthaŵi yabwino tonse pamodzi.

Lembani zifukwa ziŵiri zimene tiyenera kuphunzira za moyo wa Khristu.

(1) ______________________________

(2) ______________________________

==========================================================================

SABATA LOYAMBA: KUBADWA KWA KHRISTU
TSIKU ŁACHIŴIRI: KHRISTU PACHIYAMBI

1. Dzulo munaphunzira zifukwa zenizeni zophunzirira moyo wa Khristu.

Lembani zifukwa ziŵiri.

(1) ______________________________

(2) ______________________________

==================================================================

2. Ndi chinthu chofunika kwambiri kwa Akhristu kuphunzira za moyo wa Khristu. Cholinga cha zimenezi ndiko kuti timudziŵe bwino Mulungu. Ndipo potero tikhoza kutsata chitsanzo cha Khristu ndi kuuza ena za Iye.

Lero tiyamba kuphunzira za moyo wa Khristu. Zimene tikhale tikuphunzira ndi izi.

(1) Khristu asanabwere m'dziko lapansi, Iye anali ndi Mulungu.
(2) Iye sanali ndi Mulungu kokha, komanso anali Mulungu.

Taganizirani bwinobwino zimenezi. Kodi mukuganiza kuti moyo wa Khristu unayamba pamene iye anabdwa monga kamwana? ____________

==================================================================

3. Tidzakambirana za zimenezi tonse pamodzi. Tayamba kuphunzira za moyo wa Khristu. Koma zimenezi sizikutanthauza kuti tikambirana za kubadwa kwake ayi chifukwa sitinafike. Moyo wa Khristu sunayambike pamene Iye anabwera pa dziko lapansi pano ayi. Iye anali wamoyo kale ngakhale asanabadwe m'Batelehemu.

Pofuna kukuthandizani kuti mumvetsetse zimenezi tengani Buku Lopatulika ndipo muwerenge pa Yohane 1:1 kulekeza ndime ya 5. Ndime zimenezi zimalankhula za Mawu. Kodi pachiyambi Mawu ameneŵa anali kwa yani?

______________________________

==================================================================

4. Pachiyambi Mawu anali ndi Mulungu. Koma Mawu ameneŵa amatanthauza chiyani m'ndime zimenezi? Kodi ndime zimenezi zimalankhula za yani? Posachedwapa pa mutu woyamba wa Yohane taphunzira kuti Mawu ndi Khristu ndipo Mawuwo ndi Mwana wa Mulungu.

Yohane 1:14:

> Ndipo Mawu anasandulika thupi, nakhazikika pakati pa ife, ndipo tinaona ulemerero wake, ulemerero wonga wa wobadwa yekha wa Atate, wodzala ndi chisomo ndi choonadi.

Mawu anasandulika thupi. Izi zikutanthauza kuti Mawu anakhala munthu. Ife tinaona ulemerero wake, wonga wa Mwana wobadwa kuchokera kwa Atate amene ali Khristu.

Kuchokera pa ndime yoyamba taphunzira kuti pachiyambi Mawu anali kwa Mulungu. Ndipo tsopano tikuona kuti Khristu ndiye Mawu. Kodi pachiyambi Khristu anali kuti?

________________________________

==========================================================================

5. Pachiyambi Khristu anali kwa Mulungu. Iye anali ndi Mulungu kufikira nthaŵi imene Iye anabadwira m'Betelehemu.

Yohane 16:28:

> Ndinatuluka mwa Atate, ndipo ndadza ku dziko lapansi; ndilisiyanso dziko lapansi, ndipo ndipita kwa Atate.

Apa mukuona kuti Yesu anati, "ndinachokera kwa Atate," kodi ndi liti limene Iye anachokera kwa Atate? Iyi inali nthaŵi imene Iye anadza m'dziko lapansi.

Kodi Khristu analipo kale asanabwere m'dziko lapansi? ____________

==========================================================================

6. Khristu ndi wosiyana ndi anthu ena. Iye anali ndi moyo ngakhale asanabwere m'dziko lino. Khristu anakhala zaka zikwi asanabwere ku Betelehemu. Iye anali wamoyo kuyambira pachiyambi. Taonaninso ndime iyi.

Yohane 1:1:

> Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali kwa Mulungu ndipo Mawu ndiye Mulungu.

Kuchokera pa ndime imeneyi, kodi Khristu anali kuti asanabwere m'dziko lino?

____________________________

==========================================================================

7. Khristu anali kwa Mulungu. Mwina inu mukuganiza kuti kodi Iye angathe kukhala bwanji ndi Mulungu asanabadwe m'dziko lino?

Ndime iyi ikuti Mawu anali pachiyambi. Ndimeyi ikunena kuti Mawu ndiye Mulungu. Khristu ndi Mulungu. Koma ife tikudziŵa kuti Khristu anakhalanso munthu. Iye anachita zimenezi ku Betelehemu. Pachiyambi anali Mulungu. Ku Betelehemu Iye anakhalanso munthu. Kotero anali Mulungu ndi munthu.

Kodi Khristu anali yani asanadze ku dziko lapansili? Kodi Iye anali Mulungu ndi munthu kapena Mulungu yekha?

____________________________

==========================================================================

8. Pachiyambi Khristu anali Mulungu yekha. Iye anali Mwana wa Mulungu. Potchula kuti Yesu Mwana wa Mulungu zimatanthauza kuti Iye ndi Mulungu. Pachiyambi Mwana wa Mulungu anali ndi Atate. Izi zimatithandiza kuti timvetsetse bwino ndime ya pa Yohane 1:1.

Yohane 1:1:

Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali kwa Mulungu, ndipo Mawu ndiye Mulungu.

Tsopano tikuona zomwe akutanthauza. Izi zikutanthauza kuti pachiyambi panali Mwana wa Mulungu. Ndipo Mwana wa Mulungu anali ndi Mulungu Atate. Ndipo Mwana wa Mulungu ndi Mulungu.

Khristu anali wamoyo wa chikhalire kuchokera pachiyambi. Kodi Khristu anali kuti asanabwere m'dziko lino?

____________________________________

==========================================================================

9. Khristu anali ndi Mulungu. Tsopano mukumvetsetsa kuti Khristu anali wamoyo pamodzi ndi Atate pamene asanadze m'dziko lapansi. Inu muli kudziŵa kuti anali ndi Atate kuchokera pachiyambi.

Khristu anali wamoyo kuchokera pachiyambi. Ngati Iye sanali munthu pachiyambi kodi anali yani?

__________________________________________

==========================================================================

10. Khristu anali Mulungu. Ndipo Iye tsopano ndi Mulungu. Iye amatchedwa Mwana wa Mulungu. Ngati inu mwadziŵa zimenezi zidzakuthandizani kuti mumvetsetse bwino magawo ofunika a Buku Lopatulika. Taonani pa ndime izi.

Yohane 8:57-58:

> Ayuda pamenepo anati kwa Iye, "simunafikire zaka makumi asanu, ndipo munaona Abrahamu kodi?" Yesu anati kwa iwo, "Indetu, indetu, ndinena kwa inu asanayambe kukhala Abrahamu ndipo Ine ndiripo."

Fotokozani chifukwa chimene Yesu ananenera zimenezi. Gwiritsani ntchito zimene mwaphunzira mphunziro limeneli.

________________________________________

________________________________________

________________________________________

11. Tidzakambirana za yankho lanu kukalasi.

Kodi Yesu anali kuti asanadze m'dziko lapansi? ______________

Kodi Khristu anali yani asanadze m'dziko lapansi? ______________

==================================================================